







# CHIYAMBI CHA UTHENGA WABWINO

Phunziro 1, July 6, 2024


"Ndipo ataperekedwa Yohane, Yesu anadza ku Galileya, nalalikira Uthenga Wabwino wa Mulungu, nanena, Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupiririrani Uthenga Wabwino!" (Marko 1:14, 15)

Uthenga Wabwino wa Marko ndi waufupi kwambiri mwa Mauthenga Abwino anayi amene amakamba za moyo wa Yesu.

Ndi nkhani yachangu, yosabisa, yamphamvu komanso yotsindikizika. Zochitika zake zokhala ngati zikuchitikadi tikuona. Simungaphonye tsatanetsatane wa chirichonse chochitika popeza zokhazo zomwe ziridi zofunikira ndi zomwe zaikidwamo.

Mwachidule, Marko ndi uthenga wabwino mu zaka za mma 2000, pomwe zonse zikuchitika mwachangu, pamene nthawi ndi ndalama. Tiyeni tigwiritse ntchito nthawiyo kuphunzira chinthu chofunika kwambiri: "Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu" ( Marko 1:1 ).






**Wolemba wa Uthenga Wabwino:**

- Mtumwi olephera.
- Wothandiza pa utumiki.

**Chiyambi cha Uthenga Wabwinowu:**

- Kukonzekera. Marko 1:1-8.
- Ubatizo. Marko 1:9-13.
- Uthenga . Marko 1:14-15.

# WOLEMBA UTHENGA WABWINO

# MTUMWI OLEPHERA

"Barnaba ndi Saulo atamaliza ntchito yawo anachoka ku Yerusalemu, atatenga Yohane wotchedwanso Marko." (Machitidwe 12:25)




Monga alaliki ena onse, Marko sanadzitchule dzina. Iye anali kamnyamata pamene zochitika zimene anafotokoza zinkachitika, zimene nkutheka anaziphunzira kupyolera mu ubale wake wapamtima ndi mtumwi Petro (1 Petro 5:13).

Amayi a Yohane Marko anali mwini wa malo ku Yerusalemu kumene mpingo unasonkhana kudzapemphera pa nthawi imene Petro anatsekeredwa m'ndende (Machitidwe 12:12).



Posakhalitsa, Barnaba ndi Saulo (amene anapita ku Yerusalemu kukapereka nsembe) anatenga Yohane Marko kupita ku Antiokeya (Machitidwe 12:25).






Ku Antiokeya, pamene Mzimu Woyera anaitana Barnaba ndi Saulo kuti akhale atumiki pakati pa Amitundu, anatenga Yohane Marko monga wothandizana nawo (Machitidwe 13:2-5).


Koma moyo wa utumiki unakhala wovuta kwambiri kwa Marko wachichepere, amene anaganiza zobwerera ku Yerusalemu (Machitidwe 13:13).

# WOTHANDIZA PA UTUMIKI


Ndatsala ndi Luka yekha basi. Mutenge Marko ndipo ubwere naye kuno, chifukwa amandithandiza mu utumiki wanga. (2 Timoteyo 4:11)


Pamene Paulo anafuna za ulendo wachiwiri wa utumiki, iye anakana kulandira Marko monga wothandizana naye (Machitidwe 15:36-38). Paulo anafunikira athandizi amphamvu, amene akanakhala chochirikiza, osati cholemetsa. Marko sanakwanire pa udindowu.





Koma, Baranaba anatsimikizika kuti Marko, yemwe anali mphwake, anali ndi kuthekera kokwanira kukhala mtumwi wabwino.  Chotero, anatenga Marko kupita naye ku Cyprus, pamene Paulo ndi Sila analunjika kwawo kwa Amwenye (Machitidwe 15:39-41).





Sitikudziwa zomwe zinachitika zitadutsa izi, koma tikudziwa kuti Baranaba anali wolondola. Kupyolera m'mau atatu amene anamutchula mumakalata ake, Paulo anafika poona Marko kukhala "wothandiza pa utumiki," wogwirizira bwino ntchito (Akolose 4:10; Filimoni. 24; 2 Timoteyo 4:11 ).



Chifukwa cha mwayi wachiwiri uwu, lero tikhoza kusangalala ndi nkhani yosangalatsa ya uthenga wabwino wa Marko.

# CHIYAMBI CHA UTHENGA WABWINOWU


# KUKONZEKERA




**"'Ndipo uthenga wake unali uwu: "Pambuyo panga pakubwera wina wondiposa ine mphamvu. Ine si woyenera kuwerama ndi kumasula zingwe za nsapato zake.'(Marko 1:7)**


Marko akuyamba ndi kutionetsera ife Mulungu pokonzekera ulendo wa Mwana wake (Marko 1:1-2; Malaki 3:1). Ulendo omwe ukuyambikira m'mabwalo a Kumwamba, omwe udzamutengere Yesu Khristu ku mtanda, kuti adzalaniridwenso Kumwamba(Marko 16:19).

Pokonzekera njirayi, Mulungu akusankha Yohane M'batizi, "liu lofuula m'chipululu" Marko 1:3; Yesaya 40:3).









Yesu asanayambe ulendo wake wopereka moyo wake chifukwa cha ife, Yohane anakonzekeretsa mitima ya anthu powatsogolera kukulapa ndi kuwaitanira kuti abatizidwe (Marko 1:4-6 ).

Anawakonzekeretsa kuti alandire Mwana wa Mulungu: wamphamvu kuposa Yohane mwini; oyenera kwambiri; ndi kuti adzabatiza ndi ubatizo wothandiza kwambiri (Marko 1:7-8)

# UBATIZO

'Pa nthawi imeneyo Yesu anabwera kuchokera ku Nazareti wa ku Galileya ndipo anabatizidwa ndi Yohane mu mtsinje wa Yorodani" (Marko 1:9)



Yesu akuyamba ulendo wake mu njira yopatsa kaso kwambiri: Mulungu Atate akumuonetsa Iye monga Mwana wake, ndipo ndipo Mzimu woyera akuwonetsera kupezeka kwake (kwa Mzimuyo) mu thupi (Marko 1: 10-11). Kuyambira pachiyambi, Yesu akusonyezedwa monga munthu waumulungu, Mwana wa Mulungu. Koma amafotokozedwanso ngati munthu :



Akubatizidwa ndi Yohane, osati Yohane kubatizidwa ndi Iye

( Marko 1:9)



Akutsogoleredwa ndi Mzimu ( Marko 1:12)



Akuyenera kuti akhale pa yekha ndi Mulungu (Marko 1:13a)



Akukumana ndi zobetchera za kuthupi (Marko 1:13c)



Angelo Akumutumikira

(Marko 1:13d)

Umu ndi m'mene Yesu akuwonetseredwa kwa ife: Waumulungu wathunthu ndi munthu wathunthu. Iye ali zonse Mpulumutsi ndi M'bale, Ambuye ndi Chitsanzo. Ndilo vumbulutso lathunthu la chikondi cha Mulungu pa anthu.

«Ulemerero umene unakhazikika pa Khristu ndi chikole cha chikondi cha Mulungu kwa ife. Umatiuza za mphamvu ya pemphero—momwe liwu la munthu lingafikire makutu a Mulungu ndi zopempha zathu kuti zivomerezedwe m'mabwalo akumwamba pamene tikupemphera kuti atithandize kulimbana ndi mayesero. Mawu amene analankhula Yesu akunena kwa munthu aliyense wokhulupirira kuti: "Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa, mwa iyeyu ndikondwera."»

EGW (In the Heavenly Places - God Has Chosen Me, January 20)

| 70 weeks = 490 years | | | |
|---|---|---|---|
| 7 weeks | 62 weeks | ½ week | ½ week |
| 49 years | 434 years | 7 years | |



# UTHENGA

*Yohane atamutsekera m'ndende, Yesu anapita ku Galileya nalalikira Uthenga Wabwino wa Mulungu nati,"* (Marko 1:14)

**Uthenga woyamba wa Yesu unakhudza mbali zitatu ( Marko 1:15 )**

**"Nthawi yafika"**

Kutchulidwa kwa ulosi wa masabata 70 ( Daniel 9:24 ).

Kuchokera pa lamulo la Artaxerxes, chaka cha 457 BC, mpaka pamene Mesiya anadzozedwa, panadutsa milungu 69 (v. 25).

Izi zinakwaniritsidwa pa ubatizo wa Yesu, AD 27. Patatha theka la sabata, AD 31, Yesu anafa (v. 27).

**"Ufumu wa Mulungu wafika pafupi"**

Lonjezo lakuti pangano la chipulumutso linali litayamba kukwaniritsidwa.

**"Lapani ndi kukhulupirira Uthenga Wabwino"**

Maitanidwe otenga nawo mbali mu pangano, povomera chikhululukiro kudzera mu chikhulupiriro mwa Yesu



Uthenga wathu wamakono ukuphatikizanso mbali zitatu izi: Nthawi yakwaniritsidwa; Yesu akubwera; ndipo tiyenera kulapa ndi kukhulupirira kuti tipite naye.

“Mtolo wa kulalikira kwa Kristu unali wakuti, “Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; lapani, khulupiririrani Uthenga Wabwino.” Motero uthenga wabwino, monga momwe unaperekedwa ndi Mpulumutsi Mwiniwake, unazikidwa pa maulosi. “Nthawi” imene Iye analengeza kuti ikwaniritsidwe inali nthaŵi imene mngelo Gabrieli anamudziwitsa Daniel. . .

Monga momwe uthenga wa kudza koyamba kwa Khristu unalengeza za ufumu wa chisomo chake, momwemonso uthenga wa kudza kwake kwachiwiri ukulengeza za ufumu wa ulemerero Wake. Ndipo uthenga wachiwiri, monga woyamba, wazikidwa pa maulosi.”

EGW (The Desire of Ages, pg. 233, 234)